**CIITANO CA MAKALATA OFUNZILA**

## 1.0 CIYAMBI

A bungwe ya Dongosolo ya Anthu pa Zamanyumba ndi Umphawi mu Zambia (PPHPZ), mogwilizana ndi Wokhala M'misakasa/m'makomboni a M'mayiko (Slum Dwellers International) ndi okondwa kulengeza ciitano ca Makalata Ofunsila Thandizo ya Ndalama Yopambana (NLGF) pansi pa ndondomeko ya Maganizo/Mawu pa Zocita Zoyenela Panyengo (VCA). Ciitano cimeneci cikupita ku anthu, magulu ndi mabungwe ang'ono-ang'ono amene sangathe kufunsila thandizo ya ndalama zopelekedwa ngakhale kuti akugwila nchito zofunika zothandizila zanyengo. Thandizo ya ndalamayi ndi ya ocita nchito zanyengo amene akufuna kukulitsa nchito yawo kapena kucitapo kanthu pakagwa masoka amwadzidzidzi.

Pansi pa mgwilizano wa Unduna wa Zacilendo wa Dutch "Mphamvu ya Mawu", World Wide Fund for Nature (WWF) Netherlands, South South North (SSN), Akina Mama wa Afrika (AmwA), SDI, Fundación Avina, ndi a Hivos anayambitsa zacitukuko za Mawu pa Zocita Zoyenela Panyengo (VCA). Colinga ca nchito yomenyela ufulu yimeneyi ndi kukweza mawu aanthu am'madela kuti acitepo kanthu pakhale nchito zabwino zanyengo komanso kupangitsa magulu a zaufulu wa anthu ndi magulu amene sali odziwika bwino akhale pakati pa njila zamakono zothetsela mavuto a zanyengo pofika m'caka ca 2025. Bungwe ya Thandizo ya Ndalama Yopambana Kwambili (NLGF), ndi cida cothandizila ndalama mu zacitukuko za VCA, colinga cake ndi kulimbikitsa kupanga zosankha kuyambila pansi kupita pamwamba ndi kuphatikizapo maganizo/mawu aanthu amene nthawi zambili samaphatikizidwapo pocita nchitoyo. Komanso ndi thandizo ya ndalama yomwe yikufuna makamaka kuika patsogolo anyanchito aku maloko kulimbana ndi vuto ya kusintha kwanyengo mu Zambia. Ikufuna kuthandiza mabungwe enieni ang'ono-ang'ono osalembetsa ndi olembetsa, mabungwe amdela, mabungwe amene Si aboma ndi mabungwe ena aliwonse.

## 2.0 THANDIZO YA NDALAMA YOPAMBANA

Thandizo ya ndalamayi ndi mbali ya zacitukuko za VCA  yimene yikupeleka ndalama zoonjezela nchito za VCA kuti iwonetse njila zoyendetsela ndalama zotsogozedwa ndi dela kusamala makamaka za ocita nchito zanyengo aku maloko. Ngakhale kuti madela wamba(apansi) ndi zigwilizano za m'madela/mabungwe ali patsogolo kugwebana n'kukumana ndi mkwiyo wa kusintha kwanyengo, zoyesa-yesa zawo sizikudziwika ndipo nthawi zambili samapasidwa thandizo ya ndalama kucokela ku boma ndi ogwila nawo nchito. Pofuna kuthandizila zoyesa-yesa za anthu zomwe nthawi zambili zimanyalanyazidwa, njilayi linakhazikitsidwa ndi wogwila nchito limodzi ndi bungwe ya VCA kuti apititse patsogolo zoyesa-yesa za anthu ammudzi. Ogwila nchito amenewa akucita nchito yabwino kwambili yanyengo koma nthawi zambili amacotsedwapo kuti apeze ndalama zanyengo cifukwa bungwe yawo si yolembetsedwa. Ndalamayi imayangana kwambili mabungwe ang'ono-ang'ono (monga magulu a Acinyamata, CSOs CBOs), magulu omenyela Zaufulu za Anthu ndi magulu amene alibe mphamvu zofunsila ndi kupeleka mawuthenga (Malipoti) pa ndalama zothandizila zoonjezeleka. Maguluwa akuimila wosunga ufulu m'delalo n'kugwila nchito zothetsela kusintha kwanyengo ku maloko; kuphatikizapo magulu a azimayi ndi acinyamata, ndi magulu a anthu olemala amene cifukwa ca nchito zawo zosakhazikika, sangathe kupeza zothandizila zina.

## 3.0 ZOLINGA

- Kuthandizila zacitukuko zamene akusamalila zotsatila za kusintha kwanyengo zikukhudza anthu m'madela ali paciopsezo mdziko m'njila yomwe yimathandizila kucitapo kanthu pa zanyengo mu mgwilizano wa madzi, zakudya, mphamvu ndi umoyo;

- Kuthandizila ndi kucilikiza kukhazikitsa njila zatsopano zothetsela mavuto am'delalo zomwe zingapindulitse madela amene ali paciopsezo komanso anthu ambili kuti azitha kusintha n’kuthana ndi zotsatila zovuta zanyengo;
- Kufikila ogwila nchito osazoloweleka komanso ovuta kuwafikila amene akuyesetsa kulimbikitsa zocita zanyengo pa mgwilizano wa madzi, zakudya, mphamvu ndi thanzi
- Kuonetsa ndi kulimbikitsa njila zina zopezela ndalama zogwilitsila nchito pa zocita zanyengo za m’mdelalo.

**4.0 ZOFUNIKILA ZINA**

- Magulu ammudzi ayenela kukhala ndi mamembala osacepela pa khumi (10)
- Gulu liyenela kukhala lakhalapo kwa miyezi isanu ndi limodzi (6).
- Magulu ayenela kuyamikilidwa ndi Wogwila Nchito Limodzi ndi VCA kapena Magulu a woyanganila amdelalo/CBOs aonetsetse kuti akugwilitsa nchito ndalama zosapitilila ZMW 50,000 pamwezi.

**5.0 KUCULUKA KWA THANDIZO YA NDALAMA**

- K67,025.00, K80,430.00 ndi K134,050.00 – Ndalama Zothandizila Pakagwa Matsoka amwadzidzi
- K67,025.00 ndi K80,430.00 - kwa magulu osavomelezeka ndi osalembetsa. Nthawi yogwilitsila nchito ndi miyezi iwili (2) mpaka inayi (4).
- K 80, 430.00 ndi K134, 050.00 - Mabungwe amene ali ndi ciopsezo cocepa ali ndi dongosolo yamphamvu. Nthawi yogwilitsila nchito ndi miyezi iwili (2) mpaka inayi (4).
- K214, 480.00 kwa mabungwe ali paciopsezo cocepa amene asonyeza zotsatilapo zake/kukhudzidwa kwakukulu kwa nchitoyo. Lingalilo lopeleka thandizo ya ndalamayi yivomelezedwa ndi kabungwe yotsogolela za VCA.

**6.0 UTALI WA NCHITO**

Nthawi yoyendetsela nchitoyi ndi miyezi inayi (4). Ofunsila ayenela kukonza njila zimene zizatsimikizila kupambana kwapang’ono mkati mwa nthawi yimene yapelekedwa ndi kukhala ndi dongosolo yokhazikika pambuyo pomaliza nchito.

**7.0 KUDZIWA MADELA**

1. Lusaka
2. Chongwe
3. Rufunsa
4. Luangwa
5. Kafue
6. Chikankata
7. Chirundu
8. Siavonga
9. Itezhitezhi
10. Lukanga
11. Mazabuka
12. Mumbwa

**8.0 ZIYENELETSO ZOFUNIKILA**

*i. **Anthu Paokha***

- Ayenela kukhala nzika za dziko la Zambia kapena okhalamo.
- Asonyeze kudzipeleka kwawo pakuthana ndi mavuto ya zanyengo yaku delalo.
- Akhale ndi ndondomeko yomveka bwino ya m'mene thandizo ya ndalamayi yidzagwilitsidwila nchito popititsa patsogolo nchito ya zanyengo ku maloko.
- Asakhale uja woyenelela kufunsila ndi kupeleka mawuthenga ya thandizo ya ndalama zoonjezeleka.

***ii. Magulu/Vigwilizano(Mabungwe)***

- Ayenela kulembetsedwa monga bungwe lovomelezedwa mu Zambia.
- Ayenela kuimila wosunga ufulu wa mdela lawo ndi kugwila nchito zothana ndi vuto la nyengo ku delalo.
- Ayenela kukhala ndi mbili yomveka bwino ya m'mene akukambilana ndi anthu am'dela komanso kutengako nawo mbali.
- Ayenela kuonetsa mphamvu kapena cidwi cokulitsa dongosolo yawo yabungwe kuti akwanilitse bwino nchito yimene akufuna.
- Sakhale ndi mphamvu zolembela/zofunsila ndi kupeleka mawuthenga la thandizo la ndalama zoonjezeleka.

**9.0 NJILA YOWUNIKILA**

Mfundo zotsatilazi zidzatsatilidwa pakuunika wofunsila

| **Ziyeneletso** | **Kufotokoza** | **Ciwelengelo 1-5** |
|---|---|---|
| Zokhudza Dongosolo ya Kusintha (TOC) ya Zambia | Izi zikutanthauza kufunikila kwa zacitukuko yomwe akufuna kapena kucitapo kanthu ku Dongosolo ya Kusintha ya Zambia ndi madela ofunika kwambili amene afotokozedwa. | |
| Zotsatila Zoopsa | Muyezo uwu umaphatikizapo kuunikila ukulu wa zotsatila zoopsa zamwadzidzidzi zomwe zacitukuko yimene yikufunsidwa yikufuna kuthetsa ndi Kuika Patsogolo kugawidwa kwazinthu pazocitika zovuta kwambili n'kuonetsetsa kuti zosewenzetsa zofunika kwambili zikusamalilidwa coyamba. Zofunika kwambili ziyenela kupita ku zocitika zimene thandizo lingapelekedwe pofuna kupewa kapena kucepetsa zotsatila za nthawi yaitali, cifukwa izi zidzathandiza kucepetsa kuwononga kwamtsogolo. | |
| Kufunikila Msanga (Mwacangu) | Mulingo uwu umanena za nthawi yimene yilipo kuti muyankhe pakagwa ngozi mwadzidzidzi kapena kucitapo kanthu panchito akufuna. Kufulumila koyenela kuti tipewe kuwononkeka kwina ndi kufunika kocitapo kanthu mwamsanga kumawunikidwa, poganizila zinthu monga mpata wa kutayika kwa moyo(imfa), zotsatila zokhudza anthu ammudzi nthawi yomweyo, komanso kufunikila kocitapo kanthu mwachangu. Pazocitika zosagwilizana ndi zocita zadzidzidzi, kunfusilako kudzawunikilidwa mogwilizana ndi nthawi yimene yapelekedwa ngati zingatheke komanso ngati palibe ngozi yimene yingacitikenso yofunika kusamalila nthawiyo. Zadzidzidzi zimene | |

| | | |
|---|---|---|
| | zimafuna kucitapo kanthu mwacangu ziyenela kuikidwa patsogolo kuti zitsimikizile kuti nchitoyo yigwilidwa bwino ndiponso yothandiza. | |
| Kucitapo Kanthu Msanga | Izi zimawunika kuthekela kwa anthu kapena madela kuti athe kuthana ndi vuto la mwadzidzidzi komanso zimene afuna kucita paokha. Zimawunikidwa ngati akufunikila thandizo loonjezela ndi kupeleka thandizo yaukatswili kapena zothandizila kuti athane ndi vutolo paokha. Ngati alibe mphamvu, kugawilidwa kwazinthu ndi thandizo kuti athetse vuto la mwadzidzidzi mpaka kuziika patsogolo. | |
| Kugwilitsila nchito Ndalama | Njila zoyendetsela bwino kwambili ziyenela kuikidwa patsogolo kuti zitsimikizile kugwilitsila nchito bwino zinthu komanso kugawa ndalama kuzinthu zimene zingathandize kwambili. | |
| Zotsatila zamphamvu | kapena muyezo wa zotsatila zimene zacitukuko zimene zikufunsidwa zingabweletse. Zotsatila za nchitoyo zingakhale monga ciwelengelo ca anthu adzakhudzidwa, ciwelengelo ca opindula, kusintha kwakukulu kwadongosolo, kusintha kwakukulu kwa ndondomeko ndi zina zotele. | |
| Kucitila Zinthu Poyela ndi Kuyankha | Wopemphayo ayenela kuonetsa mmene angagwilitsile nchito ndalama ndi kuziyendetsa momwe anasonyezela. Izi zimatsimikizilidwa ndi macitidwe osamalilila ndalama amene akonzedwa. | |
| | **Total** | |

**10.0 ZOCITA ZOSAYENELA KUKAMBILANA**

- Zocita zimene zimalimbikitsa tsankho, kudyela anthu masuku pamutu, kapena kuwononga cilengedwe, anthu, kapena madela sizidzaganizilidwa.
- Zocita zosemphana ndi malamulo kapena zophwanya malamulo a mdela lanu sizingakhale zoyenela.
- Zocita zongoganizila cabe zofuna za ndale kapena zipembedzo sizingakhale zoyenela.
- Nchito zimene sizigwilizana ndi zolinga za "Next Level Grant Facility" kapena kulephela kuthana ndi vuto ya kusintha kwanyengo yaku maloko siidzaganizilidwa.

**11.0 NJILA YOFUNSILA**

Zolemba zotsatilazi ziyenela kudzazidwa molingana ndi malangizo amene apelekedwa pamwamba kapena mkati mwa zipepala.

1. Zigawo (fomu) zofunsila Thandizo ya Ndalama Yoyenelela/kanema yosonyezedwa ndi zigawo zofunsila/ Zigawo olembedwa ndi manja m’Cinyanjanja, Cibemba kapena Citonga
2. Zolemba za Bungwe za msonkhano watha. Izi ziphatikizepo mamembala amene akuvomela kupempha thandizo ya ndalama.
3. Kalata ya ciyamikilo kucokela ku mpingo, atsogoleli ammudzi, atsogoleli asukulu ndi zina zotelo.
4. Zigawo zolembetsela ngati nkotheka.

**12.0 M’MENE MUNGAFUNSILE**

Tengani ndi kudzaza Zigawo imene ipezeka apa. Tsatilani malangizo mosamala ndi kulemba Zigawo.

Phatikizani zipepalazo monga mwasonyezedwa, kenako tumizani pa mphepo kapena tumizani kudzela pa imelo pphpz@outlook.com kapena kupeleka pamanja ku ofesi kapena tumizani ku adilesi iyi:
Attn: Woyanganila Thandizo ya Ndalama,
PPHPZ
P.O. Box 36202
Lusaka,
Zambia.

Mabungwe angathe kutumiza mafunso kuti afotokozele momveka bwino isanafike 1 October, 2024, nthawi ya 23:59hrs, kudzela pa imelo pphpz@outlook.com / info@peoplesprocess.org kapena kugwilitsila nchito pa mphepo. Gulu ya VCA lidzayankha mafunso onse pofika 12.00hrs pa 2 October 2024 ndi kuwaika patsamba ya webusaiti ya VCA kuti onse amene angafune kulembetsa apeze cidziwitso.

## 13.0 KEYALA YOKAMBILANA

Peoples Process on Housing and Poverty in Zambia
P.O.Box 36202
Email:pphpz@outlook.com & info@peoplesprocess.org
Nambala ya Foni: +260 761363 634

## 14.0 NTHAWI YOMALIZA KUPELEKA

Zigawo (Mafomu) ofunsila Thandizo ya Ndalama ayenela kudzazidwa mu Cingelezi, Cinyanja, Cibemba kapena Citonga ndipo ndondomeko yofunsilayi idzatsegulidwa kuyambila 23 September 2024 mpaka pa 5 October 2024. **Tsiku yomaliza kufunsila** ndi 5 October 2024 ndipo ofunsila amene asankhidwa adzatumilidwa uthenga pa 11 October 2024. Kugwilizana(kupatsidwa) za nchito kudzayamba pa 22 October 2024 ndipo kugawila ndalama kudzacitika pa 23 October 2024 ndipo Kukhazikitsidwa kwa nchitoyi kudzacitika m'miyezi inayi.

## 15.0 MAWU A M'CITIDWE WA ZIPHUPHU

Kupempha kulikonse kapena kukopa kapena kuyesa ciphuphu kapena kusonkhezela Am'mgwilizano wa VCA, Ogwila nawo Nchito a VCA, ofisala (nyanchito), kapena wotsogolela, zidzacititsa kuti pempho yanu ya thandizo ya ndalama kukulepheletseni. Pempho lililonse laciphuphu kwa gulu ya osankha liyenela kupelekedwa ku imelo yathu ya wovumbula ciphuphu: complaints@vca.com ndipo mfundo zoteteza wovumbula ciphuphu zidzatsimikizika. Kutengako mbali kwanu poyankha ciitano cino sizikutsimikizila kuti mupeza thandizo ya ndalama. A bungwe ya PPHPZ ndi Am'mgwilizano wa VCA ali ndi ufulu wopeleka kapena kusapeleka thandizo ya ndalama yiliyonse panthawiyi.

## 16.0 ZIGAWO (MAFOMU) OFUNSILA

1. Zigawo (Fomu) zofunsila mukhoza kuyapeza pano.
2. Zigawo za Bajeti/Dongosolo za Ndalama ipezeka pano.
3. Kuunika kwaciopsezo kupezeka pano.

17:0 ONLINE APPLICATION
BEMBA:
https://formlink.solstice.world/#/9961eada2b384bfb96351e8e8efc3e52/60d0dc032b654ff887318458d0bd39ce?branding=solstice

Tonga:

https://formlink.solstice.world/#/ee1d1aa18e77474aaf003e552559dd2d/cfb7f6e1674f434bab7c7e168732
0dd5?branding=solstice

NYanja:

https://formlink.solstice.world/#/d9597d93a1154124956b4b27062d656a/5822991e7b6d4f15b03ff910c4
b141ce?branding=solstice

English:

https://formlink.solstice.world/#/f824a6e6fb7f44b1aa654162fd398d7e/3dec6062090d426382081b7f653
1ead5?branding=solstice